www.xtrapapers.com

M11/1/A1CHW/SP1/NYA/TZ0/XX

22110055

International Baccalaureate®
Baccalauréat International
Bachillerato Internacional

**CHICHEWA A1 – STANDARD LEVEL – PAPER 1**
**CHICHEWA A1 – NIVEAU MOYEN – ÉPREUVE 1**
**CHICHEWA A1 – NIVEL MEDIO – PRUEBA 1**

Wednesday 11 May 2011 (morning)
Mercredi 11 mai 2011 (matin)
Miércoles 11 de mayo de 2011 (mañana)

1 hour 30 minutes / 1 heure 30 minutes / 1 hora 30 minutos

---

INSTRUCTIONS TO CANDIDATES

- Do not open this examination paper until instructed to do so.
- Write a commentary on one passage only. It is not compulsory for you to respond directly to the guiding questions provided. However, you may use them if you wish.

INSTRUCTIONS DESTINÉES AUX CANDIDATS

- N’ouvrez pas cette épreuve avant d’y être autorisé(e).
- Rédigez un commentaire sur un seul des passages. Le commentaire ne doit pas nécessairement répondre aux questions d’orientation fournies. Vous pouvez toutefois les utiliser si vous le désirez.

INSTRUCCIONES PARA LOS ALUMNOS

- No abra esta prueba hasta que se lo autoricen.
- Escriba un comentario sobre un solo fragmento. No es obligatorio responder directamente a las preguntas que se ofrecen a modo de guía. Sin embargo, puede usarlas si lo desea.


© International Baccalaureate Organization 2011

www.xtrapapers.com



*Lembani ndemanga pa nkhani **imodzi** mwa nkhani ziwiri zili m'munsizi.*

**1.**

Tili pano anthuni ndi pamaliro. Onani gulu la anthu ankhope zachisoni kuzungulira nyumbayi. Tamvani amayi kulira mochita kulandirana ngati kuti ndi kanyimbo, koma kuli kumva ululu wobereka. Mwati miyezi isanu ndi inayi nkukhala chibwana? Iyayi mpake kulira. Musamangomva kuti kuli chikuta kudziko kuno, kubala nkovuta.

Kodi nanga Chautayu wagwera pa ndani?

Mwana wa a Mbwana dzina lake Kondwani watisiya. Anthu akuti waphedwa, koma ena akuti wadzipha. Kaya timve ziti pamenepa?

Eee! Tamvani, khalani chete ndiye ngati tate wake wa mwana wotisiyayu akulankhula m'nyumbamu.

"… Tisananyamuke kupita kumanda ndati ndikuuzeni abale kuti kuliraku ine pano ndikungolira chifukwa chakuti wamwalirayu ndi mwana wanga. Kunena zoona sindine woyenera kulira chifukwa cha imfa ya mwana uyu."

Tonse tidang'ung'udza kuoentsa kusagwirizana ndi zomwe ankalankhula anamfedwawo.

"… Mudziwa bwino kuti imfa n'zosiyanasiayana; anthu amafa chifukwa cha matenda kapena ngozi, koma imfa ya mtundu uwu ndiyochita kuiputa dala, ndiponso yochititsa manyazi. Kunena zoona munthu yemwe afa m'njira iyi siwofunika kumulira koma poti ndi munthu wamzimu ndiye choncho tiyenera kumulira."

Tidang'ngudzanso chifukwa ambiri sitinkadziwa kuti a Mbwana ankalankhula chiyani. Omwe ankadziwa amangogwedeza mitu kuonetsa kugwirizana ndi mawuwo.

Amuna awiri adathamangira m'nyumbamo kukawatonthoza a Mbwana, koma panthawiyo iwo sanali woti n'kutonthozeka mwamsanga.

Adatuluka panja akupukusa mutu. Amuna awiri aja adawalondola kukawauza kuti nthawi yopita kumanda inali pafupi, koma iwo adakana kuti sanali wokozneka kupita nawo kumandako. Pambuyo pake atawanyengerea adavomera.

Tidanyamuka ulendo wa kumanda. Monga adanenera tsiku la maliro lija a Mbwana anali okonzeka kulongosola bwino za mwana wawo uja.

"… Ndichinthu chowawa kukhala ndikumakambabe za mwana wanga Kondwani pomwe iye sali moyo, koma poti ndifuna kuti ana ena atolepo phunziro ndiganiza ndibwino kulongosola zonse.

Anthu ena akhala ndi mwayi wokhala ndi ana ambiri m'banja, koma ine chifukwa chodwaladwala kwa mkazi wanga Mulungu adandipatsa ana awiri okha, wamwamuna, Kondwani, ndi wamkazi, Mavuto. Ndidafunitsitsa kuti ana awiriwa aphunzire bwino, koma chifukwa chosowa ndalama ndidaganiza kuti Kondwani poti ndiye anali wamwamuna aphunzire kuti mtsogolo muno atisunge, ndikutinso adzamuthandize mlongo wakeyo.

Panalitu zovuta zambiri kuti mwanayo aphunzire chifukwa chakuti nthawi yakale chitukuko chisanafike kwathu kuno. Panthawiyo wotumiza mwana kusukulu ankasekedwa kwambiri kuti ankangotaya nthawi pachabe. Anthu ankati sukulu yeniyeni ndiye kutumiza mwana ku ubusa.

Kondwani atayamba sukulu alamu wanga adadza kudzandifunsa ngati zinali zoona zomwe adamva kwa anthu.

"Ndamva kuti mwamuyambitsa sukulu mwanayu. Kodi ndizoona zimenezi?"

"Inde ndamuyambitsadzi sukulu."

"Chifukwa chiyani mwachita zimenezi?"

"Kumukonzera mwana wanga moyo wamtsogolo."

www.xtrapapers.com



"Hahahahahaa! Eti, kumukonzera moyo wamtsogolo. Alamu sindikuseka ayi. Ngati muli ndi nzeru musiyiretu zomwe mwayambazi. M'malo motumiza kusukulu mwanayu muyenera kumamuphunzitsa ntchito za pano panyumba."

"Ntchito za panyumba n'zosavuta, ndidzimuphunzitsa akaweruka kusukulu."

"Ndikumva chisoni ndi mwanayu chifukwa mungofuna kumutayitsa nthawi pachabe."

Ndidakalipa. "Chonde ndisiyeni musandivute. Bwanji nthawi zonse mumakonda kulowerera nkhani za m'nyumba mwanga ngati kuti mulibe yanu nyumba? Muyenera kuchita manyazi. Tulukani m'nyumba mwanga muno." Ndidakalipa.

"Mpaka kundipirikitsa."

"Inde, ndikuti tulukani m'nyumba mwanga muno." Nditatero alamuwo anatuluka mokwiya.

Mwana wanga Kondwani yemwe anali wokonda kufunsafunsa adandifunsa chifukwa chiyani ndidapirikitsa amalume ake mwachipongwe chonchija.

"Amalume ankalankhula zopusa."

"Zopusa zotani bambo?"

"Amati ndikusiyitse sukulu."

"Inde inu abambo ankanena zoona amalumewo. Nanga taonani zigamba ine chonchi; m'malo moti mukanandigulira kabudula wabwino inu nkutenga ndalama kukalipira kusukulu. Ndiponso nthawi yomwe ndizikhala kusukulu anzanga azikhala kuubusa. Aa! Bambo mungofuna kunditayitsa nthawi. Sindikufuna sukulu yanuyi. Anzangatu ayambapo kale kundiseka ngati chitsiru.

Nthawi yomweyo ndidamugwira mwanayo nkumulanga molimba kufikira adagwira mwendo kuti ndimukhululukire. Ndidamusiya ndipo ndidamuuza kuti atuluke m'nyumbamo.

Willie Zingani, *Ndaziona Ine* (1981)

– Fotokozani njira kapena luso limene mlembi wagwiritsa ntchito pofuna kusonyeza chikhalidwe kapena zikhulupiriro za anthu amene ali mu nkhaniyi.

– Fotokozani momwe mlembi akusonyezera udindo wa amayi mu nkhaniyi.

– Fotokozani luso limene mlembi wagwiritsa ntchito pofuna kusonyeza khalidwe la anthu amene ali mu nkhaniyi.

www.xtrapapers.com



**2.**

**Likongolerenji Bokosi?**

Likongolerenji bokosi,
Monga loseketsa,
Wolipanga analipanga,
Kulipangira misozi.
Akonzeranji chosakondweretsacho?
Wochilandirayo naye sachikana,
Likongolerenji bokosi,
Monga losangalatsa.

Wolipangayo salifuna,
Koma alipangiranji?
Wokhalamo salidziwa,
Nanga achitamonji?
Wolinyamula sakondwa nalo,
Tsono alinyamuliranji?
Olitsata liwaliritsa misozi,
Nanga alitsatiranji?
Wochipanga sachifuna,
Wokhalamo sachidziwa,
Ochinyamula sakondwera nacho,
Ochitsata chiwaliritsa – bokosi la maliro.

E J Chadza, *Ntchito ya Pakamwa: Ndakatulo za m'Chichewa* (1963)

– Fotokozani maganizo anu pa luso la mlembi logwiritsa ntchito "mafunso" mu ndakatuloyi ndipo mufotokoze momwe mafunsowa akutha ndizira kuti ndakatuloyi imveke bwino.

– Maluso a zolembalemba monga ndakatulo amathandiza anthu owerenga kuganiza mozama. Perekani ndemanga yanu malinga ndi ndakatuloyi.

– Kodi ndani akuyankhula m'ndakatuloyi ndipo akupereka uthenga wotani?